


MATENDA NDI ZOSAUTSA

 Ine ndikufuna kufotokoza chinachake, zinthu zina zofunika kuti inu muzidziwe. Mawu anga siali ofuwula kwambiri, kotero ine mwina ndiyenera kufika cha *apa*. Ngati Ambuye alola, Lamlungu madzulo, ine ndikufuna kulankhula kwa inu mwa ulaliki wakufalitsa Uthenga, wa Lamlungu madzulo. Ndipo ife tikuyembekezera zinthu zina zazikulu, kuti Ambuye atichitire ife sabata ino.

² Chinthu chimodzi chiri chokhudza...ambiri pano sakanakhoza nkomwe kumvetsa chabe momwe kuti makadi apemphero awa ama—amaperekedwera kwa odwala ndi osautsika. Mu zaka zitatu zakuyesera, ili ndilo dongosolo lokhalo limene ine ndinalipezapo lomwe linali kwenikweni lowoneka ngati linali lodalitsidwa ndi Mulungu.

³ Poyambapo ife timakhoza kungolowamo ndipo osakhala ndi makadi konse, nkungowaleka anthu akhale pa mzere. Kunali kuchulukana kwake, nakonso. Ndiye ine ndimafika popemphera mwina khumi ndi asanu, maminisi makumi awiri nthawi zina; unyinji umakhoza kundiwunjilira ine, ndipo iwo amachita kuzandisololapo ine.

⁴ Ndiyeno potsatira, tinayamba, ife timatumiziratu makadi apemphero kwa atumiki. Ndipo mtumiki aliyense wothandizira, mwinamwake mipingo makumi asanu kapena kupitirira mdera lonse imakhoza kuthandizira msonkhano, ndipo mtumiki aliyense amakhoza kukhala ndi makadi osachepera zana limodzi. Mtumiki aliyense amafuna mpingo wake poyamba. Iye amakhoza kuwapereka iwo kwa mpingo wake ndipo nkutheka usiku unayi wonse kapena usanu, mpingo wa mtumiki mmodzi yekha umakhoza kulowamo, ena otsalawo amakhoza kuyipidwa nazo kwambiri.

⁵ Ndiye ife tinaganiza za kukhala ndi anthu wamba, anthu wamba chabe oyandikirapo; ndipo nthawi zina anthu amabwera mwa kuchuluka monga mitunda zikwi zisanu ndi ziwiri, zisanu ndi zitatu ku misonkhano. Izo sizinali zabwino.

⁶ Ndipo njira yokhayo imene ife tinayipeza yoti ife tikanakhozadi kulora Ambuye kupanga njira, ndiyo kudza ndikutenga makadi a pemphero, pafupi makumi asanu aiwo, ndikungowapereka iwo ku magulu a anthu, ndipo palibe wina akudziwa chabe ndani ati akhalemo.

⁷ Ine ndawona nthawi imene ine ndapereka makadi makumi asanu popanda ndi imodzi yomwe ya iwo kuitanidwa. Kuyamba mu msonkhano, ndipo Mzimu wa Ambuye kungonditsogolera ine pakati pa anthu, chotero, ngakhale osagwiritsa nkomwe ntchito makadi opempherera.

⁸ Ine ndaona nthawi yomwe ine ndimakhoza kukhala ku nsanja, ndikungoyamba kulankhula, ndipo ine ndikungodziwala ine yense kwa ora limodzi kapena kupitirirapo, nthawi, m'mene ndikuitana mmodzi woyambayo, ndipo kenako winanso chotero. Ndinka...Aliyense kuchiritsidwa.

⁹ Anthu ambiri amalimbira pa—pa mzereno. Ine ndinachita ndemanga iyi, ndi yowona, zakhala bwino kwa zaka zisanu... kwa zaka zitatu tsopano. Ndikhululukireni ine. Munthu aliyense wodza ku nsanja kuno akuchiritsidwa. Sipanakhalepo konse chinachake, ziribe kanthu chapotolozedwa moyipa chotani, chopunduka, kapena chosautsidwa, nthawizonse chimachiritsidwa. Pakhala zina zochititsa mantha. Koma ine... Mwinamwake, mu nthawi ya usiku umodzi, ine ndikanakhoza kutenga mwina atatu kapena anayi kapena asanu. Mwina nthawi zina...

¹⁰ Ine ndinaona kamodzi ku Calgary, Canada, iwo anatenga awiri okha, kumene anthu zikwi makumi awiri ndi zisanu anasonkhana. Awiri.

¹¹ Mmodzi anali mnyamata atasautsidwa kwa zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu, dzanja lake linali lopinimbira. Iye anali mu chikuku. Amayi ake anapinyolitsa mphete yawo ya chikwati, kuti amusunge iye. Iye anakhalapo mmisonkhano isanu ndi iwiri kapena isanu ndi itatu; sanathe kupeza khadi. Potsiriza nthawi yake inafika kuti iye akhale ali pa nsanja. Mnyamatayo anayenda pochoka pa nsanja. Mmawa wotsatira, iye anadzimeta yekha kwa nthawi yoyamba mmoyo wake. Anakumana nane kunjako podikirira ndege pomwe ndege inatera ku Vancouver, kuti andigwire chanza.

¹² Msungwana wamng'ono anali wotsatira. Msungwana wamng'ono, M'katolika mwa chikhulupiriro, mwendo umodzi unali ma inchesi anayi kufupika mosiyana ndi unzake. Ife tinali ndi pafupi ora limodzi ndi chinachake tiri ndi msungwana wamng'ono ameneyo. Ndipo Baibulo lomweli... Pamene iwo anamubweretsa iye kumeneko, iye amakhoza kupita kutali kumbali. Ine ndinasanjika Baibulo ili pamutu pake, iye anayenda bwinobwino monga mwana aliyense, uku ndi uko akuyenda pa nsanja, pamene anthu zikwi makumi awiri ndi zisanu atakhala, akuonerapo. Koma, zinthu zimenezo, ife tikungonena.

¹³ Ine sindikudziwa wina muno amene ali ndi khadi la pemphero, kapena amene ati akhale woyamba. Ife timapereka makadiwo ndiyeno ife timalowa mkati.

¹⁴ Ine ndiyesa kukupatsani inu lingaliro. M'bale wanga akuti, "Ine ndinapereka makadi makumi asanu."

15 Ine nkulowa nchinyumbachi, ine mwina ndikumana ndi mwana wamng’ono. Ine ndikanakhoza kunena, “Ungathe iwe kuwerenga?”

Nkuti, “Inde, bwana.”

Ine ndinena, “Yamba kuwerenga.”

16 Mwinamwake iye akhoza kuwerenga mpaka khumi, khumi ndi zisanu kapena makumi awiri, ndi kulekeza; paliponse iye walekezerapo, ine ndimakhoza kuyambira mzere wa pemphero. Ngati iye walekezera pa makumi awiri, ine ndimakhoza kuyambira mzere wa pemphero pa makumi awiri, ndipo mwina kumapita mtsogolo kapena chammbuyo.

17 Mwina usiku wotsatira ine ndikanakhoza kuwerenga anthu angapo mu mzere ndikugawa pawiri, ndi kuona kuti ndi nambala yanji yomwe ili, kapena chinachake monga choncho.

18 Palibe amene akudziwa pakalipano, usiku uno, pamene mzere wa pemphero uti uyambire; pamene pati paoneke ngatipo basi. Nthawi zina zimagwera pakati pa olumala pomwe. Nthawi zina zimagwera pakati pa odwala. Ine sindikudziwa. Palibe wina akudziwa. Ife timangopereka khadi ndipo kenako kuwalola Ambuye atsogolere kotsalirako, ndipo nthawizonse zagwira bwino ntchito mosalephereka mwa njira imeneyo. Khalani mu pemphero.

19 Ine ndikukhulupilira izi zonse ndi zatsopano kwa inu anthu pano. Mu misonkhano yonse yomwe ine ndakhalamo, uwu ndi msonkhano waung’ono kwambiri wa usiku wachiwiri womwe ine ndakhala nawo mu msonkhano uliwonse chiyambire ine kukhala mu ntchitoyi. Kawirikawiri, pa usiku wachiwiri, malo akulu a msonkhano aliwonse, kapena utalengezedwa mulimonse, kawirikawiri amathamangira zikwi zisanu ndi ziwiri, zisanu ndi zitatu, khumi, pofika usiku wachiwiri. Chifukwa, wangolengezedwa cha konkuno basi. Chimene chimapanga unyinjira, ndi chifukwa zimalengezedwa mmaiko akutali, ndipo mazana ochuluka chotero amachokera mdziko limodzi, ndi mmaiko ena, kudzapanga gulu.

20 Msonkhano wanga wotsatira tikatha kuno ukakhala ku Houston, ku bwalo la masewero. Ine ndikuganiza kumakhala anthu zikwi khumi ndi zisanu ndi ziwiri, ine ndikuganiza. Ziri kale pafupi mu mapepala anayi kapena asanu ofika kumayiko akutali. Uko ndi kumene anthu amachokera, kutsidya kwa nyanja zazikulu ndi konse, kulikonse.

21 Ine ndikukhumba kuwerenga gawo lochepa chabe la Mawu usiku uno, pakuti Mawu a Mulungu samalephera konse. Mawu anga akhoza; Mawu Ake sangakhoze. Iwo akupezeka mu Masalimo 103, ndime ya 1, ya 2, ndi ya 3.

Dalitsa AMBUYE, O moyo wanga: ndi zonse ziri mkati mwa ine, dalitsa dzina lache loyera.

Dalitsa AMBUYE, O moyo wanga, ndi kusaiwala zokoma zake zonse:

Amene akhululukira mphulupulu zako zonse; amene achiritsa nthenda zako zonse;

²² Mulungu atawonjezera madalitso Ake kwa Mawu Ake! Zonse za izi, kulankhula za *Matenda Ndi Zosautsa*, ine ndikukhumba kwa mphindi zochepa chabe kupanga maneno ena okhudza ichi. Ndipo ine ndikufuna inu mumvetserere ndi kulipatsa ilo tcheru chanu chosagawanika.

²³ Matenda ndi zosautsa zonse ndi zotsatira za tchimo, mwina osati mu moyo wanu, koma mu moyo wa winawake inu musanakhalepo. Mdierekezi ndiye m'yambitsi wa matenda ndi zosautsa. Ife tisanakhale ndi Mdierekezi aliyense, ife tinalibe matenda kapena zosautsa. Koma, pamene Satana anadza, iye anabweretsa palimodzi naye matenda ndi zosautsa.

²⁴ Pali nthawi zambiri pamene ife timanena za izo ngati madalitso. Ine sindikanaganizapo kuti Mulungu akanakhoza kupeza dalitso kuchokera kwa munthu wodwala; pokha akanakhala wochimwa, pomulondolera iye kwa Mulungu; kapena mwana wosamvera, kumubwezeranso iye kuti akayanjanitsidwe kwa Atate ake. Koma matenda ndiwo zotsatira za Mdierekezi ndi za kugwako. Uje. . .

²⁵ Lero, ife tiri ndi madotolo opambana kwambiri amene takhala nawo. Ife tiri ndi sayansi ya mankhwala yopambana, zipatala zopambana zomwe takhala nazo; ndi matenda ambiri kuposa omwe ife takhala nawo. Ndipo mu tsiku limene tiri ndi sayansi ya mankhwala yopambana yomwe ife takhala nayo, iwo akungopitirirabe kumanga malo a osachiritsika. Pamene pomwepo ife tiri ndi ntchito ya sayansi yopambana kwambiri pa zosautsa ndi matenda yomwe ife takhala nayo; kumanga kosungirako, pachaka, kwa osachiritsika.

²⁶ Koma panalibe chinthu chomwe chinadza pamaso pa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, koma chomwe Iye anali woposa kukumana nacho. Ndipo Iye ali chimodzimodzi lero monga Iye analiri dzulo, ndipo adzakhala kwa nthawizonse. Ndipo Iye amatsikimizira zimenezo. Ndipo inu murchiona icho, usiku ndi usiku. Ndipo ngati sichiri choncho, ndiye inu muli ndi ufulu wa kukaika.

Winawake anati, “Kodi machiritso amatha?”

²⁷ Iwo amatha pomwe chikhulupiriro chathera. Koma pamene chikhulupiriro chilephera, ndiye machiritso anu adzalephera. Kodi inu munganene munthu aliyense amene anadza kuguwa ndi kutembenezidwa kuti angakhale Mkhristu masiku ake onse? Iye akanakhoza kukhala usiku uno mwana wa Mulungu, ndipo mawa kukhala mwana wa Mdierekezi. Ndi pamene iye ataya chikhulupiriro mwa Mulungu, chomwe chimamubwezera iye m'mbuyo.

28 Ndipo mphamvu iliyonse yomwe ikanakhoza kukuchizani inu pano pa nsanja ino ikhoza kukusungani inu bwino. Ndi chifukwa chake ine ndinapanga mfundo iyi, kuti, palibe chomwe chimadza pano koma chimene chikuwomboledwa pano. Kuchoka pano, zimatengera chikhulupiriro chanu ngati chingakhazikike.

29 Ine ndawonapo anthu akudza ku nsanja, akhungu kwathunthu, nawerenga Baibulo lomwe ili. Mu masiku ochepera asanu, kubwerera kunonso akhungu basi monga mmene iwo analiri. Chifukwa chiyani iwo anawerenga pano? Mphamvu ya Mdierekezi inazindikira mphatso ya Mulungu iyo ndipo iye anayenera kuchoka. Tsopano izo ndi zo-. . .izo ndi a. . .Ine ndikudziwa imeneyo ndi mfundo yeniyeni yoti nkuipanga, koma ine ndikudziwa pamene ine ndayima. Ndipo ine ndikudziwa Yemwe ine ndamkhulupirira, ndipo ine ndikudziwa mphamvu Yake yochiritsa.

30 Winawake anati, si kale pamene ine ndinali mu Phoenix. Mizere yapemphero inafika mpaka mu misewu; iwo sakanakhoza ngakhale kulowa mochitira msonkhano. Popita mu mzere, winawake anati, “Kodi—kodi iwe sukuwopa, M’bale Branham, kuima pamenepo pamaso pa zinthu zonsezo ndi kuzindikira kuti otsutsa ayima pomwepo ndi atolankhani a nyuzipepala, ndi ena otero, kuti atsutse?”

31 Ine ndinati, “Ine sindiwopa bola ngati ine ndikumverera kuti Iye ali pafupi. Koma ngati ine sindingakhoze kumumverera Iye, ine ndikanatsika pa nsanja ndikupita kunyumba.”

Palibe munthu angakhoze kuchita kanthu. Zonse ziyenera kubwera kuchokera kwa Mulungu.

32 Mwachitsanzo, ife titenge. . .kukamba mwa mphindi pang’ono za khansara. Iyo ikuoneka ngati imodzi mwa adani akulu lero. Kodi khansara ndi chiyani? Kodi iyo inachokera kuti? Chotupa, khungu, nsungu, chibayo, chifuwa chachikulu, onse a mayina amenewo ali maina a zamankhwala amene asayansi ya za mankhwala anawapatsa iwo. Baibulo limawaulula iwo kuti ndi ziwanda. Mwachitsanzo, khansara, kodi khansara ndi chiyani? Nthawi zambiri imachokera pa kusupuka.

33 Zinthu zonse zachirengedwe za padziko zimayimira zauzimu. Chirichonse mu chirengedwe chimayimira chauzimu. Inu mukudziwa zimenezo, ambiri a inu nonse.

34 Mwachitsanzo, monga pamene mwana abadwa, ndi pamene mwana abadwa kwa Mulungu. Pamene mwana, pamene mwana abadwa mu Ufumu wa Mulungu. . .Baibulo linati, “Pali atatu amene achitira umboni kumwamba, Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” [Winawake wakhala akufuula, nthawi zingapo—Mkonzi].

³⁵ Tsopano, ndi wina akudwala kapena chinachake, kotero ingondipatsani ine tcheru chanu. Ngati inu mungaphonye zinthu izi, inu muphonya mwina machiritso anu, palimodzi.

³⁶ “Alipo atatu amene amachitira umboni kumwamba.” Tsopano, pamene ife tiri...Kutembenuka kwathu. Chinthu chinachokera mu thupi la Yesu Khristu pamene Iye anafa; pamene panali madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo zinthu zitatu izi zimapanga Kubadwa kwatsopano. Kodi izo nzolondola, atumiki? Zinthu zitatu izi zimapanga Kubadwa kwatsopano; madzi, Magazi, ndi Mzimu.

³⁷ Izo zimapanga kubadwa kwa chirengedwe, pamene mwana abadwa. Chinthu choyamba ndi chiyani? Madzi, magazi, moyo. Zinthu zonse za chirengedwe zimayimira zauzimu.

³⁸ Ndipo khansara, mwa chirengedwe... Mu zauzimu, iye ndi Mdierekezi. Iye amayimira khwangwala ndi mwimba; zimadya zinthu zakufa.

³⁹ Khansara amachokera posupuka. Mwachitsanzo, dzanja langa, ilo—ilo—ilo liribe khansara aliyense pa ilo. Ndipo ilo mwina likhoza kukhala, nthawizina. Chabwino, chimayambitsa khansara nchiyani? Ndi ka...Khungu lina, nyongolosi mu thupi langa, limabwerera mmbuyo, limasupulidwa, kapena chinachake kulowamo. Ndipo kuchokera ku nyongolosiyo, kapena khungu, iyo imayamba kuchulukitsa kwa makungu, kuchulukitsa, ndipo izo zimayambitsa khansara ndipo izo zimayamba kudya mkati mwa thupi.

⁴⁰ Tsopano, moyo uliwonse, ndi kagawo kalikonse ka moyo komwe kalipo, kanabwera...kamabwera kuchokera ku nyongolosi. Inu enianu ndinu ochokera ku nyongolosi ya moyo. Inu munabwera, nthawi yina, inu munalikanyongolosi chabe kakang'ono kwambiri, tating'ono chotero ito sitikanakhoza kuwoneka ndi maso a chirengedwe. Inu munachokera kwa bambo wanu. Inu simuli kanthu, mulibe magazi a mayi wanu mpang'ono pomwe. Khungu la magazi limachokera kwa munthu wa mwamuna. Ndiyeno kuchokera ku nyongolosi imeneyo, ilo limakhala likuchulukana makungu. Ndipo chirichonse mwa mtundu wake; nyongolosi yochokera mwa galu idzabala galu, yochokera mwa mbalame mbalame, ya munthu munthu. Ngati palibe chosokoneza zimenezo, dongosolo la Mulungu, palibe chosokoneza ilo, icho chidzabala mwangwirowi, mwana wabwinobwino. Ndipo iye adzakula kudzakhala wangwirowi, mkulu wabwinobwino, ngati palibe chomwe chingamusokoneze iye. Koma pamene pali china chosokoneza icho, ndiye chikhala kuti ndi choyipa chimene chimasokoneza dongosolo la Mulungu.

⁴¹ Mulungu sanalinge inu kuti mukhale odwala. Mulungu anakupangani inu mwa mafanizidwe Ake. Iye akufuna inu muzikhala muli bwino. Iye anachita chirichonse chimene Iye angathe kuti akusungeni inu bwino.

42 Ndipo Satana akutsutsana ndi inu. Koteru, khansara uyu iye—iyu imayamba, kapena chotupa ichi, chirichonse chomwe chiri, kuchokera mu nyongolosi iyo imayamba kuchulukana, monga chotupa kukhala chachikulu, zina zotero. Ilo ndi thupi, monganso inu muli a thupi. Iyo ili ndi mzimu monganso inu muli mzimu, chabe iyo ilibe solo. Koma iyo ili ndi moyo monga inu muli ndi moyo. Ndipo chotero, ndiye, mwa inu, mu thupi lanu, muli miyoyo iwiri. Umodzi ndi inu ndipo winayo ndi chinthu china, makungu ochulukana, kumakula thupi, monganso inu munakulira mwa thupi. Kodi izo nzolondola?

43 Chabwino, ndiye, chinachita zimenezo ndi chiyani? Mdierekezi. Nyo—nyongolosi ndi moyo. Poyamba, nyongolosi ndi kakhungu kakang’ono kali ndi moyo mkati mwake. Ndipo moyo umenewo ungabwere kuchokera ku magwero awiri okha, mwina kuchokera kwa Mulungu kapena kwa Mdierekezi. Ndipo inu munachokera ku nyongolosi ya moyo, mwa Mulungu. Khansara, chotupa, kapena zina zotero, kuchokera mu nyongolosi ya moyo mwa Mdierekezi. Ndipo iye akuyesetsa kuwononga moyo wanu. Iye amadya mtsinje wa magazi anu ndi—ndi njira zosiyana iye amagwira ntchito pa inu. Koteru, ine ndikudziwa kuti iwo ali adierekezi. Yesu Khristu anawatcha iwo adierekezi. Ndipo chomwe Iye anena ndi choonadi. Iwo ali mdierekezi. Mdierekezi ndi wozunza. Iye ali pano kuti aling’ambe thupi lanu, kukudyani inu psyiti, kukuwonangani inu, kufupikitsa zanu “makumi asanu ndi awiri,” ngati iye angathe.

44 Ndicho chifukwa chake kuti pamene Mngelo uyu wa Mulungu atsikira kumene ine ndiri...Ine sindikudziwa kanthu za aliyense wa inu. Koma ndicho chifukwa chake Iye amakuwuzani inu mtundu wa matenda amene inu muli nawo mu thupi lanu, chifukwa moyo umenewo ndi womvera kwa Moyo umene Mulungu wawutumiza pansu kudzazindikira izo. Ndiye potero zinthu zimene inu mwachita mu moyo wanu. Izo zachitika mwa mphanvu ya Mulungu, ndiye ine ndikhoza kudziwa ngati ziri pamenepo kapena zachoka. Ndipo inu mukhoza kuziwona izo mwa zotsatira zowonetseredwa mwathupi. Inu mukhoza kuwona wodwala, pamene thupi lake likhala lowongoka ndi labwino, maso ake amatseguka, kapena makutu ake amakhala osagontha.

45 Tsopano icho ndi chiyani? Inu mukuti mwamuna, monga mnyamata wamng’ono pano, kapena ine ndikukhulupirira ena a inu munalu ku Kachisi uko usiku ungapo wapitawu kukawona. Pano pali chithunzi cha kumene a *Chicago Tribune* anapereka, za osalankhula asanu ndi anayi, amene iwo anawatumiza kumeneko, amene anachokera kosungirako anthu, obadwa ogontha ndi osalankhula, mmodzi wa iwo wosamva, wosalankhula ndi wakhungu. Tsopano mwina ena mwa mabwana anawerenga zolembazo kwa inu. Tsopano anthu amenewo, manyuzipepala monga *Chicago Tribune*, siali

otengeka ayi. Matenda oterowo amafufuzidwa kwathunthu mwamtheradi iwo asanayikidwe mu pepala chotero, a *Waukegan Sun*, kapena *Post Dispatch*, kapena ina mwa mapepala amenewo. Sindiko kutengeka ayi. Izo sizongodzipangitsa, chikhulupiro chopeka, kapena lingaliro. Izo ndi Nyonga za Mulungu Wamphamvuzonse. Ndipo Iye alipano kuti atsimikizire Izo usiku uno, ndipo achita izo. Ndipo osonkhana athu akangofika mwamsanga pokhala ndi lingaliro limodzi ndi mtima umodzi. . .

⁴⁶ Ngati ili—ngati gulu ili la anthu lakhala pano, makamaka iwo amene ati apemphereredwe usiku uno, kubwera ku nsanja, ngati iwo ati adzakhale mwa mtima umodzi ndi chiyanjano chimodzi; mu mphindi zisanu zikubwerazi chabe, sipakhala mmodzi wa iwo mu zikuku izi kapena mmachira. Ngati iwo ati adzakhulupirire kuti ichi ndi Choonadi. Ndipo pamene iwo akubwera, mmodzi ndi mmodzi, usiku uno, ku nsanja; ngati iwo ali, aliyense payekha, akapanda kuchotsedwamo mu zikuku zimenezo ndi mmachira ndi zinthu, nayenda pochoka ku nsanja ino, bwinobwino, ndiye inu mukhoza kunena kuti ine ndi wolakwa.

⁴⁷ Ndipo ine ndizibwezera kwa Mulungu, Amene, Iye ndi wosalephera. Inu muchiritsidwa. Tsopano Iye ali pano kuti apangitse Mawu Ake kukhala abwino. Mawu aliwonse amene Mulungu anena ndi wona. Koma inu muyenera kusakhulupirira iwo mwatheka; inu muyenera kuwadziwa iwo.

⁴⁸ Anthu ena amabwera, kumati, “Ine ndikukhulupirira.” Iwo amaganiza kuti akukhulupirira; koma ngati inu mukanapeza mmodzi mu chikwi chirichonse amene akukhulupirira kwenikweni. “Chikhulupiro ndicho thunthu la zinthu zoyembekezeka, umboni wa zinthu zosawoneka.”

⁴⁹ Ife timalamuliridwa, matupi athu ndiwo, mwa mphamvu zisanu. Ndi angati akudziwa zimenezo kuti nzoona? Tiyeni tione manja anu. Mphamvu zisanu; kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva. Zimenezo zimalamulira munthu wachibadwa.

⁵⁰ Tsopano pali munthu wina mkati mwakemo, amene ali munthu wa chikhulupiro, mzimu. Iye ali ndi mphamvu ziwiri. Imodzi ya izo ndi chikhulupiro, inayo ndi kusakhulupirira. Zimene, zikupanga nambala yangwiyo ya Mulungu, zisanu ndi ziwiri, mphamvu zomwe inu muli nazo.

⁵¹ Tsopano, pafupi yense wa inu muno mukanakhoza kulumbira zedi mwa mphamvu zanu zisanuzo. Tsopano zindikirani ichi m’kamphindi chabe.

⁵² Kodi inu mungayime pano, kamphindi kokha, Dr. Cauble? Tsopano ine ndikukhulupirira kuti pali mwamuna amene wayima patsogolo pangapa, wavala suti yaying’ono yamawanga-mawanga, wavala magalasi, ndi taye yofiira. Ndi angati

akuganiza kuti ine ndalondola, tiyeni tiwone manja anu? Chabwino, inu mukudziwa chotani kuti pali mwamuna amene wayima pamenepo? Chifukwa inu mukumuona iye. Kodi izo nzolondola? Tsopano iyo ndi njira yokhayo, mphamvu yokhayo, imene ine ndiri nayo tsopano ikanakhoza kundiwuza ine paliwina amene wayima pamenepo, chifukwa ine ndikumuona iye. Kupenya kukufotokoza za iye.

⁵³ Chabwino, ine sindikumuwona iye tsopano, koma ine ndikukhulupirirabe kuti iye ali pamenepo. [M'bale Branham atembenuza mutu wake kwa M'bale Cauble, koma amugwira iye—Mkonzi.] Tsopano inu mukuti, “Kulankhula ndiko kukhulupirira.” Ndi choncho? Ine ndikukhulupirira kuti Dr. Cauble wayima pamenepo tsopano, ndipo ine sindikumuwona iye. Chifukwa, ine ndatengedwa ndi mphamvu yapayokha, kunja kwa kupenya; iyo imatchedwa kukhudza, ndipo ine ndikumverera kuti iye ali pamenepo. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndi Dr. Cauble. Sikuti ndi Dr. Bosworth. Chifukwa, Dr. Cauble anali ndi Chipangano chaching'ono mu dzanja lake, ndipo ilo likanali pamenepo. Kotero ine...?..Ine ndinalankhula motero nthawi imodzi ndipo winawake anabweretsa wina kwa ine. Koma ine ndinazindikira kuti Dr. Cauble ali ndi Baibulo laling'ono ili mu dzanja lake, ndipo ndi Dr. Cauble. Tsopano njira yokha yomwe ine ndikanakhoza kudziwa kuti iye anali atayimirira pamenepo tsopano ndi mwa mphamvu ya kukhudza. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndi zoon.

⁵⁴ Koma tsopano ine sindikumukhudza iye ayi konse. Mphamvu imeneyo ndi yakufa kwa ine, koma ine ndikudziwa iye ali pamenepo chifukwa ine ndikumuona iye. Mukuona chomwe ine ndikutanthawuza?

⁵⁵ Pali mphamvu ziwiri zodziwika za thupi zimene zikuti iye alipo. Imodzi mwa izo, ine ndikumuwona iye. Yotsatira yake, ine ndamukhudza iye. Tsopano apo zimachitika. . .

Tangoyimani pamenepo mwakamphindi chabe, m'bale.

⁵⁶ Tsopano ine ndiri ndi mphamvu ina, ndipo iyo ndi ya kumva. Yimbani nyimbo ya chinachake. [Wapiyano ayamba kuyimba—Mkonzi]. Ndi angati akukhulupirira pali nyimbo ikuyimbidwa? Tiyeni tiwone manja anu. Kodi inu mukuyiwona iyo? Ndi angati akuyiwona nyimboyo? Kodi inu mwainunkhiza iyo, kuilawa iyo, kuikhudza iyo? Chabwino, nanga inu mwadziwa bwanji kuti ndi nyimbo? Inu muli ndi. . .Bwanji ngati wina akanakhala alibe izi—mphamvu ya kumva tsopano mkati muno? Iwo sakanakhoza kudziwa kuti nyimbo ikuyimbidwa; mphamvu imeneyo ndi yakufa kwa iwo. Iwo sakanakhoza kuyimva iyo, chifukwa iwo sangathe kumva. Koma inu amene muli ndi mphamvu ya kumva mukudziwa kuti iyo ikuyimbidwa chifukwa inu mukuyimva iyo. Inu simungakhoze kuyiwona iyo, inu simungaikhudze iyo,

inu simungayinunkhize iyo, inu simungayilawe iyo, koma inu mukhoza kuyimva iyo.

⁵⁷ Tsopano chikhulupiriro ndicho thunthu la zinthu zoyembekezedwera, umboni wa zinthu zimene iwe siwukuziwona, kuzilawa, kukhudza, kununkhiza, kapena kumva. Koma mphamvu ya chikhulupiriro yangokhala yeniyeni monga kuwona kwanu kuliri, kapena iliyonse ya mphamvu zanu. Kodi inu mukuwona zomwe ine ndikutanthawuza? Inu khulupirirani izo, inu mungo...Palibe wina amene angakupangitseni inu kuti mukayikire icho, chifukwa inu mwagwidwa ndi mphamvu imeneyo yomwe ikukuwuzani inu kuti ziri choncho.

⁵⁸ Inu mukanakhoza kunena, “Malaya awo anali woyera.” Bwanji ngati ine ndikanakuwuzani kuti iwo anali ofiyira? Chabwino, inu simungakhulupirire izo, chifukwa iwo ndi ojera. Mphamvu yanu ya kupenya ikuti ndi ojera. Maso anu akutero.

⁵⁹ Chabwino, tsopano ngati inu mukukhulupirira, inu pano oti mupemphereredwe, kaya ndinu ndani, ngati inu mukukhulupirira usiku uno kuti inu muchiritsidwa, molimbika chabe monga kuwona kwanu kukunenera kuti malaya awo ndi ojera, ntchito yachitidwa pakali pano.

Zikomo inu, Dr. Cauble.

⁶⁰ Izo nzolondola. Chikhulupiriro ndicho thunthu la zinthu zoyembekezedwera, umboni wa zinthu zimene inu simukuziwona, kuzilawa, kuzikhudza, kuzinunkhiza, kapena kuzimva. Iyo ndi mphamvu yina. Izo ziri mu kachitidwe kena. Iyo sichina chachibadwa.

⁶¹ Inu simungakhale ndi chirichonse kuchokera kwa Mulungu, mwa chikhulupiriro chokha. Mwa chikhulupiriro makoma a Yeriko anagwa. Mwa chikhulupiriro Mose anakana kutedwa mwana wa mwana wamkazi wa Farao. Mwa chikhulupiriro Gidioni anachita zakuti-nzakuti. Mwa chikhulupiriro, njira yokhayo!

⁶² “Ndipo popanda chikhulupiriro ndi kosatheka kumukondweretsa Mulungu.” Ndipo ngati inu mukufuna kumukondweretsa Iye, inu muyenera kubwera kwa Iye ndi chikhulupiriro, kukhulupirira Mawu Ake kuti ali Choonadi.

⁶³ Chifukwa chiyani ine ndikuyima ndi kumalankhula mawu awa chotere ndi kunena kuti palibe chomwe chingabwere ku nsanja kuno popanda icho kuwonedwa ndi kudziwa nthendazo, zinsinsi za mitima? Ndipo ziribe kanthu zikhale zopunduka moyipa chotani, palibe wina aliyense, amene anakhalapo mu misonkhano yina, koma akudziwa kuti nthawi iliyonse iwo amachiritsidwa. Motani? Pamene Mngelo anakumana nane, Iye anati, “Ngati ungachititse anthu kukhala owona mtima...” Kapena, “Ngati iwe udzakhale woona mtima ndi kuwachitisa anthu kukukhulupirira iwe, palibe chomwe chiti chidzayime

pamaso pa pemphero lako.” Ine ndikukhulupirira izo. Ndipo ngati ine ndingachititse inu kuchita chinthu chomwecho; Louisville, Kentucky adzakhala ndi kugwedeza monga komwe sanakhale nako kalelonse. Icho ndi chitsutso.

⁶⁴ Koma chomwe ine ndikuyesa kuchita, usiku uno, ndi—ndi kukutangani inu kuti muwone chomwe ine ndikutanthawuza. Ndiye pamene inu mubwera pano, ndi kuwomboledwa, yimani pa Mawu amenewo. Iye—Iye ali Wansembe Wamkulu wa kuvomereza kwanu. Mulungu sangachite kanthu kwa inu mpaka poyamba inu muvomereze kuti Iye ali. Ndiye pamene inu muvomereza icho, ndiye khulupirirani icho, chitani pa icho ndi kukhala nacho, ndipo Mulungu adzakutulutsani inu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Mpingo unena, “Amen.”—Mkonzil Zoonadi.

Pano osati kalekale . . . ku Fort Wayne, Indiana.

⁶⁵ Pajanso, ine ndiri ndi chonena chochepa pamenepo, Dr. Bosworth, mu thumba la bulandi langa, iwo adzabweretsa icho kwa inu, za m—m msonkhano womwe ife tangochokerako, mu *We The People*. Ine ndikukhulupirira anali msungwana wamng’ono wakhungu, umene iwo anawulengeza. Zibwera mu *We The People* tsopano, bukhu lomwe limapita mu dziko lonse, za mtolankhani wa nyuzipepala amene analemba mawu otsutsa, anati, “Msungwana ankadzinerera kuti iye anali atachiritsidwa, ndipo sanali.” Ndipo msungwanayo ali ndi zimene adokotala ananena, ndi zina zotero choncho, ndipo anazifalitsa izo. Ndipo kenako iwo anafufuza izo, ndipo tsopano zapita ngakhale ku *We The People*. Mulungu adzasuntha, ndipo palibe wina amene angakhoze . . . Ine ndilola Dr. Bosworth akuwerengereni inu izo, mwina, mu msonkhano wa mawa madzulo. Izo zangotumizidwa kumeneko ndi—ndi pepala ya ku Fort Wayne kumtundako.

⁶⁶ Akazi a Bosworth, mu msonkhano; iwo amangopitiriza, ena a iwo amati . . . Panali mwamuna atakhala kumeneko ndi kusokonezeka kwa misempha kochuluka, anali wopuwala kwa zaka khumi. Ndipo iye anali ndi kupuwala koyenderera, kunabwera mpaka mu nsana wake. Iye anali bambo wa malonda wa mzindawo. Ndipo iwo sankadziwa . . . Iwo anamkhazika iye pamenepo. Ndipo iwo anali atawona ambiri mu zikuku, ndi anthu ovutika, akuwomboledwa. Ndipo usiku umenewo, msungwana wamng’ono wa maso otembenuzika kumbuyo kwa nyumbayo anali atawona anthu ambiri akuwomboledwa, maso-otembenezika.

⁶⁷ Ine sindinawone mwana wa maso-otembenezika aliyense atabwera ku nsanja yemwe sanachiritsidwe. Ndipo ife tawona oposa mazana atatu a maso-otembenezika, akuchiritsidwa, nthawi yosakwana miyezi isanu ndi umodzi. Ife tinali nazo zolembedwa za izo. Mawumboni zikwi makumi anayi kwa

odwala, mpaka tsiku, la kuchira, maumboni, osayinidwa ndi madokotala, ndi ena otero.

⁶⁸ Ora lafika, anthunu. Nthawi ili pano. Ine ndikunena izi, ndipo inu mukhoza kunditcha ine wotengeka, ngati inu mungafune kutero. Ine ndikukhulupirira kuti izi zikusonyeza Kubwera kwachiwiri kwa Yesu Khristu. Amen. Pakuti, kudzakhala zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndipo chinthu chake ndi chakuti, ngati inu simuli mu Ufumu wa Mulungu, limbikirani kulowa Imo. Ndithudi ine ndikhoza kukhala ndi kudziwa kwina kwa chomwe ine ndikuchilankhula, kapena Mulungu sakanamakhoza kulemekeza pemphero langa kuchita zomwe Iye amachita. Ndipo inu kunja kwa Ufumu, funani Khristu monga populumukirapo panu tsopano, pamene ili nthawi ndi pamene inu muli ndi mwayi.

⁶⁹ Ine sindidzayiwala maneno. Nthawi yina ine ndinali nditayimirira ku . . .

⁷⁰ Pajatu, kuti nditsirize kukuwuzani inu za msungwana wamng'ono ku Fort Wayne. Akazi a Bosworth anamuwuzwa iye, nati, "Wokonedwa . . ." Iye anali kugulitsa zowerenga, mmbuyo kumbuyo kwa nyumbayo.

⁷¹ Iye anabwera kumeneko, akulira, nati, "Akazi a Bosworth," amenewo ndiwo akazawo a M'bale Bosworth, nati, "Ine ndawona anthu otembenuka-maso onsewo akuchiritsidwa," iye anali mayi wamng'ono, pafupi khumi ndi zisanu ndi zitatu, maso-otembenuka mowopsya. Nati, "Ngati inu mungadze . . ." Nati, "Ngati ine ndikanangolowa mmenemo ndi kukhala mu mzere wa pemphero! Koma ine sindingakhoze ngakhale kupeza khadi."

⁷² Akazi a Bosworth, mwachifundo, anapita kwa mwanayo. Iwo anati, "Wokonedwa, ngati iwe ungapite cha kumbuyo uko kumene iwe ungate kumamuona iye, ndipo kwenikweni . . . Usa—usangolingalira chabe tsopano. Koma khulupirira ndi mtima wako wonse kuti imeneyo ndi mphatso ya Mulungu, ine ndikukutsimikizira iwe iye akuyitana iwe mu mphindi zochepa."

⁷³ Ine ndinali kupempherera odwala pa nsanja, nsana wanga ndinali nditatembenukira kwa msungwanayo. Mwa nthawi imodzi, ine ndinamverera icho chikukhazikika mkati, chikhulupiriro chikusuntha. Ine ndinayang'ana pozungulira, ine sindikanakhoza kuchilondola, panali ochuluka kwambiri atangoyima mopanikizana. Ndipo ine ndinadziwa kuti chikuchokera kumeneko, ndipo ine ndinayesera kuzindikira kuti ndi mtundu wanji wa mzimu womwe unali. Onani, chikhulupiriro chake chinasuntha mpaka mu gulu loterolo.

⁷⁴ Ndipo pamene ine ndinatembenuka, potsiriza ine ndinamupeza iye. O, kawiri utali wa nyumbayi, kupawona pamene iye anali. Iye anali atavala kotho lobiriwira. Ine ndinati, "Mkazi wamng'ono wayimirira kumbuyo uko, ali

ndi maso-otembenuka, ndi kotho lobiriwira, usawopenso ayi. Mulungu wakuchiritsa iwe.” Maso ake anakhala angwirowinobwinobwino. Icho ndi chimodzi chokha cha zochitika zikwi zomwe zachitika njira imeneyo.

⁷⁵ Tsopano pamene, ngati ife tingakhale ndi msonkhano, ngati inu anthu mungabwere palimodzi ndi kungotaya zimene inu mumaganiza kuti ndi *izi, izo*, ingoziponyani izo kumbali. Osabwera kudzangowonera chabe. Bwerani mukukhulupirira ndipo muone ngati zinthu zomwezo sizichitika pompano mu nyumba muno.

⁷⁶ Nthawi yoyamba, pamene ine ndinakumana ndi Dr. Bosworth, kuno, munali mu Miami. Ife tinali ndi msonkhano. Dr. Bosworth, wodziwika kumaiko, zaka makumi anayi wozindikira kuphunzitsa za machiritso Auzimu. Iye ankaganiza kuti tsiku lina Mulungu adzatumiza m—mphatso kwa mpingo. Ndiyeno pamene iye anamva kuti ine ndinali kumeneko, iye anangoganiza, “Chabwino, ndi zimenezonso uko, winawake kularikira chabe machiritso Auzimu.” Iye anabwera ku msonkhano usiku umodzi. Ndipo kubwera chopoyola mu msonkhano...Ife tinali ndi, chimene iwo amatcha, nzere wofulumira; zikwi zinali zitayimirira.

⁷⁷ Madzulo amenewo, anyamata awiri aang’ono a WBAY, nyumba yowulutsira mawu, pokhala akufunsidwa, pokhala atabadwa akhungu. Onse awiriwo analandira kupenya kwawo, ndipo iwo anali nawo iwo kumeneko ku nyumba yowulutsirako mawu, akuwafunsa.

⁷⁸ Koteri M’bale Bosworth anabwera ku msonkhano. Ndipo zinachitika kuti, pamene nzere wofulumira unayamba, apo panali zikwi zingapo zoti zidutsepo usiku umenewo; popanda kanthu koma kungosanjika manja pa iwo akamadutsa, anayi mbali ndi mbali.

⁷⁹ Iwo anamukankha msungwana wamng’ono chomupyoletsa. Ine sindidzamuyiwala mwanayo. Iye anali kanthu kakang’ono kosangalatsa. Iye anali wamng’ono, msungwana wa tsitsi la golide; dzino limodzi loguluka pa mphumipa; ndipo anali pang’ono, athira zonyezimiritsa zatsopano pang’ono mu tsitsi lake, kapena zomwe inu mumadzitcha zinthu zomwe akazi amayika mu tsitsi lawo. Iwo anamukankha iye...iye anali atavala zothandizira poyenda, mmusi mwake mwa—mwa chiuno chake apa. Ndipo iwo amachita kumamukankha iye popyola mu mzere, ndipo ine ndinasanjika manja pa iye. Iye amakhoza kuchoka pa nsanja, ndipo iwo amamukankhiranso iye mu nzere. Bwanji, chinthu chaching’ono chosawukacho! Ndipo iye ankangobwerabe napyola. Ndiyeno wina amakhoza kumubweretsa iye chopoyola, ndipo iwo amasanjika manja pa iye. Ndipo pamene msungwanayo ankadutsa kenanso,

iyе anayang'ana mmwamba, kukhala ngati kumwetulira kwakung'ono kuja, inu mukudziwa, ndi dzino limenelo palibe.

Ndipo Chinachake chinangoti, “Muylimitse mwanayo.”

⁸⁰ Ine ndinati, “Wokonedwa” Ine ndinawona kuti iye analibe chikhulupiriro choti nkuchiritsidwa nacho pa nthawi imeneyo.

⁸¹ Koma, onani, iyo ndiyo ntchito yake ya mphatso. Pano pa nsanja, inu mungazindikire momwe Iye, nthawizina, inu mumachita kugwira ntchito. Anthu kuti, “O, ine ndikukhulupirira, M'bale Branham.” Koma iwo ali apa, pansi *apa*; ndipo apa ndi pamene iwo ayenera kukhala, pamwamba *apa*. Chabwino, ndiye zinthu izo za kuwauza matenda awo ndi zinsinsi za mu mtima wawo, chikhulupiriro chimakwera mpaka ine ndimamufikitsa munthuyo pondikhulupirira ine.

⁸² Icho ndi chomwe Iye ananena, “Ngati iwe ungachititse anthu kukukhulupirira iwe, ndiye khala woona mtima pamene iwe ukupemphera, palibe chiwanda chingagwire mpaka pamenepo, ndiye.” Iye ayenera kudziwa Mbuye wake. Ndiye. . . Ndipo ine ndikudziwa Iye anandiiza ine zimenezo.

⁸³ Ndipo pamene ine ndikhoza kutengera wodwalayo kufika pa malo pamene mpaka chikhulupiriro chawo chingafike apa, ndicho chomwe chimandipatsa ine chikhulupiriro changwiro. Ine sindinachiwonepo icho chikulephera. Ndipo icho sichidzalephera. Icho sichingalephere.

⁸⁴ Ndiyeno pamene msungwanayo, iwo anamukankha iye chopoyola, ine ndinati, “Wokonedwa, iwe yima kumbuyo kwanga komweku.” Ndipo iye anayima kumbuyo kumeneko, nditangomugwira iye, iye anagwirira mapeto a kotho langa. Ine ndinati, “Iwe zipemphera, wokonedwa.” Ndipo iye amakhoza kuwelamitsa mutu wake waung'ono pansi, kupemphera.

⁸⁵ Ndipo M'bale Bosworth anali atakhala, kusunga zonsezi mkati, komabe wokayikira pang'ono basi. Ndipo iye amangopenyerera, chifukwa iye anali kunjja uko, kumangopenyerera msonkhano wotsiriza ukupita kwakutha. Ndipo iye anali. . .Uwo unali usiku wotsiriza, ine ndikukhulupirira unali.

⁸⁶ Ndipo iye anali atagwirira kotho langa, ndipo ine ndinangopitirira kupemphera. Ine ndinali nditayiwala za mwanayo. Ine ndinatembenuka kachiwiri, ine ndinati, “Wokonedwa, pitiriza kupemphera,” monga choncho.

⁸⁷ Ndipo patapita nthawi, ine ndinayamba kumverera chikhulupiriro chimenecho chikuyamba kukhazikika mkati, monga kugunda kwa mtima, gu, gu, gu. Ndipo pamene icho chinayamba ku. . .[Malo osajambula pa tepi—Mkonzi]. . . kupitirira chotero, ine ndinatembenukira kwa iye. Ine ndinati, “Tsopano, wokomamtima,” ndipo ine ndinasanjika manja anga pa iye ndipo ndinawafunsa Ambuye Yesu.

Ine ndinati kwa mayi, ine ndinati, “Tsopano chotsani zomuthandizira poyendazo pa iye.” Iye anati, “Koma, M’bale Branham, ine ndikukuwuzani inu, iye . . .”

⁸⁸ Ine ndinati, “Musakayikire inu zimenezo, mayi. Inu chitani zomwe mwauzidwa kuti muchite.” Iye anayenda napita kumeneko nakachotsa zothandizira mwanayo poyenda.

⁸⁹ Uyu akubwera apayunso ndipo atagwirizira zothandizira poyenda zazikuluzo, kwa anthu amenewo chotero; alibwino mwangwiro, bwinobwino monga momwe iye akanakhalira, miyendo yaying’ono imeneyo. Kodi izo nzolondola, Dokotala Bosworth? [M’bale Bosworth anena “Amen.”—Mkonzil Ndipo anapitiriza nawo msonkhano. Mphindi zochepa zokha, ine ndinapitiriza . . .

⁹⁰ O kawiri utali wake, kapena mwina kuposera, wa nyumba iyi, pansa pa hema yozungulira yayikulu pomwe anthu anali atayimilira, kukafika kunja kumbuyo mpaka mu misewu yaikulu, uko ku Princess Gardens. Ndiye mpaka mmbuyo, ine ndinapitirira . . .

⁹¹ Ine ndinamverera chinachake chikukhazikika mkati, kuyamba kuteronso, “fyuu, fyuu.” Ine ndinadziwa icho chinali chikhulupiriro. Ine sindikanakhoza kudziwa chabe kumene icho chinali kuchokera. Ine ndinkangotembenukabe, kuyang’ana; koma anthu amadutsa mofulumira kwambiri, ndipo iwo akulira, kuyesa kukukhudza iwe ndi zinthu.

⁹² Patapita kanthawi, ine ndinachiwona Ichu, kutali chakumbuyo uko, mwamuna atavala malaya oyera. Ine ndinayembekezera, kupeza kaye mtundu wanji wa mzimu umene unamumanga iye. Mwamunayo anali wopunduka. Iye anali woti anagwa pa kavalu, zaka zingapo izo zisanachitike. Anali wamalonda mu Miami. Dzanja lake linali lopunduka, ndipo mkono wake, monga *choncho*. Iye anabwera uko monga wotsutsa, kudzatsutsa mu msonkhanowo. Ndiyeno iye anayamba kukhala ndi chikhulupiriro.

⁹³ Ine ndinayima ndipo ndinati, “Bwana, inu kumbuyo komwe uko, wachinayi kuchokera mu mzere, kubwerera mmbuyo mbali *iyi*, muli ndi malaya oyera mmwambamu, mwavala, yimirirani pa mapazi anu. Yesu Khristu wakuchiritsani inu.” Ndipo pamene iye anayimirira, manja ake anakwera mmwamba. Kamkazi kake kali pakepake, inu mukanaganiza kuti ndi wodziyeretsa, monga m’bale wamng’ono ananenera izi mmawa uno pa kuwulutsa mawu kwake, kumumva iye akufuula. Iye anali pamene, wowomboledwa mwangwiro.

⁹⁴ M’bale Bosworth anafufuza nkhanayi, ndiye iye anabwera kwa ine. Iye anamufunsa munthuyo zonse za izi. Ndipo pamene iye anabwera kudzazipeza izi motere, iye anati, anandifunsa ine, nati, “Iwe unadziwa bwanji kuti ameneyo anali munthuyo?”

⁹⁵ Ine ndinati, “Bwana, ine ndinayamba kufooka. Ine ndinadziwa kuti zikuchokera kwinakwake.”

⁹⁶ Ndipo iye anati, anapita ku cholankhulirapo, iye anati, “Izo zikutsimikizira Yesu Khristu kukhala yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Izi zikutsimikizira izo.” Nati, “Tsopano, mphatso yomwe inali mwa Yesu Khristu ikanakhoza kukhala nyanja iyi yonse kuno, kumenyana ndi gombe. Mphatso mwa m’bale wathu ikhoza kukhala ngati supuni yodzadza ndi madzi otungidwa mwa iyo. Koma zopangitsa zomwezo zikhoza kukhala mu supuni yodzadza ndi madzi, mtundu wa zopangitsa womwewo ndi womwe uli mu nyanja yonse.” Izo nzolondola.

⁹⁷ Ndipo ine—ine ndimakhoza kudzimva ndikuyamba kutopa. Ndipo apo panali bambo atawomboledwa mwangwiro.

⁹⁸ Tsopano izo zachitika mazana a nthawi. Ndipo pali anthu mu nyumba ino, ine ndikukhulupirira, amene akhalapo mu misonkhano ina, kuti achitire umboni. Kodi ine ndiri ndi anzanga pano amene akhalapo mu misonkhano ina, angachitire umboni nanena kuti izo nzoona? Kwezani manja anu ngati inu muli pano. Tsopano inu mukhoza kuwona. Baibulo linati “Mwa pakamwa pa awiri kapena mboni zambiri.”

⁹⁹ Tsopano, pamene, inu mukhoza kukhala ndi chinthu chomwecho kuno mu Louisville. Palibe chifukwa choti wina aliyense achoke pano wopanda kuwomboledwa mwangwiro. Ine mwina sindingakhale ndi nthawi kwa aliyense pa nsanja, koma aliyense akhoza kupindula nawo. Ngati Mulungu angadzitsimikizire Iyemwini pano kuti ali Mulungu, ndi chomwe chatsimikiziridwa chomwe ine ndanena kuti ndi choonadi, ndiye khulupirirani Mulungu. Koteri chitani pa chikhulupiriro chanu, ndi kuyika chikhulupiriro chanu monga mchitidwe wamoyo, ndipo Mulungu adzachita ntchito pa inu pomwepo, ndipo adzakukhalitsani bwino inu.

¹⁰⁰ Hot Springs, tsopano, kunali . . . Ine ndikukhulupirira kunali ku Little Rock. Usiku wina magalimoto otenga matenda anali ambiri, mpakana anatsekereza msewu wa magalimoto. Iwo anachita kubweretsa polisi kumeneko kudzachotsetsa iwo ku ngodya imeneyo, cha kumunsi kwa nyumba yaikulu mu Hot . . . mu Rock . . . Little Rock, Arkansas.

¹⁰¹ M’busa Bambo Brown anali mmodzi wa abusa kumeneko. Ngati inu mukufuna kupeza umboni uwu, lemberani kwa M’busa G.H. Brown, 505 Victory Street, Little Rock, Arkansas, ndipo mverani kwa uwu. Kulankhula za mphamvu ya ziwanda! Ndipo chabe . . . Uwo unali msonkhano wanga wachinayi kapena wachisanu, cha mma leveni koloko; dzanja langa linachita dzanzi kwambiri.

¹⁰² Nthawizina pamene ine ndikupita kunyumba, dzanja langa limachita dzanzi kwambiri, mopitiriza, mpaka ine nditalithowa ilo ndi madzi otentha kwa pafupi theka la ora, kuti lifike

pakuti kumverera kubwererenso pa ilo, kuchokera mwathupi. Ndipo pali wotchi; ine ndimagwira manja a anthu, nditavala iyo pamenepo, izo zimayimitsa wotchi imeneyo zii mwakufa. Ine ndiri ndi wotchi ya Longines tsopano, yongochokera kumene ku fakitale. Ine ndinayigwira iyo. Sizochitika zake mwathupi, kapena mwazitsulo zomwe izi zinachita kwa iyo, ine sindikudziwa ayi.

¹⁰³ Koma Bambo Brown anati, “Bwerani titsikire mu chipinda chapansi, M’bale Branham, kolankhulirako.” Iye anati, “Ine ndiri ndi nkhanu pansipa imene inu simunawonapo chinthu chirichonse monga icho.” Chabwino, ine ndinatsikirako pamene ndinali kupuma.

¹⁰⁴ Ine ndawonapo zinthu zowopsya, koma ine sindinawonapo chinachake kwenikweni chonga icho. Ine ndinapitapo kowetera anthu kumene akazi aang’ono amagwiritsa ntchito zokozeramo, kumazola pa nkhope zawo, misala. Ndaonapo zinthu zowopsya, koma popanda china monga ichi. Atagona pansu anali mkazi wa pafupi zaka makumi atatu, makumi atatu ndi zisanu, mkazi wa maonekedwe amphamvu. Ndipo iye—miyendo yake inali atayikweza mmwamba monga *chonchi*, ndipo iyo inali ikuukha magazi.

¹⁰⁵ Panali mwamuna atayimirira pa masitepe, m’bale wabwino chabe wokalamba wa ku Arkansas atavala ovololo, ndi shati ya buluu. Ndipo, anzanga, ine nditi, nthawi zina mitima yabwino kwambiri imagunda mkati mwa zimenezo. Izo nzolondola. Izo nzoona, ine ndikukhulupirira. Ine—ine sindimakonda zodzipangitsa zirizonse. Ine—ine ndimakonda amuna ndi akazi achikale enieni, izo nzolondola; opulumutsidwa ndi Mulungu, obadwa kawiri. Ndipo iye anali atayimirira pamenepo, atavala zovala zake za maonekedwe ofwifwa. Ine ndinati . . . Ndinapita pansipo.

Ine ndinati, “Muli bwanji inu?”

Ndipo iye anati, “Usiku wabwino. Kodi ndinu M’bale Branham?” Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Nati, “Ine ndimaganiza kuti ndi inu.”

¹⁰⁶ Cholankhulirapo chimamveketsera izi mkati umo pansiponso. Iwo anali ndi gulu la amisala mbali imodzi.

¹⁰⁷ Koma iwo sakanakhoza kumusunga mayi uyu ndi wina ayi. Zinatengera pafupi amuna asanu ndi atatu kapena khumi kuti amulowetse iye mkati. Iwo amalephera kubwera naye mu ambulasi. Iwo amalephera kumulowetsa iye mu ambulasi. Ndipo iwo anatumiza winawake kumeneko mu galimoto, ndipo mayiyo anaswa magalasi onse a galimotoyo, ndipo amuna amenewo kuyesera kumugwirizira iye mu galimoto. Ndipo apo iye anali, atagona chagada. Dokotala anali atamulasa ndi mankhwala. Kusintha kwa moyo wake asanakule kunamufikitsa mu izi. Ndipo apo iye anali, atagona chagada.

108 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndituluka ndikawone ngati ndingamve kunjenjera kulikonse.

109 Iye anati, “M’bale Branham, inu musapite kumeneko.” Nati, “Iye akhoza kukuphani inu.”

Ine ndinati, “O, ine sindikuganiza ayi,” chotero basi.

110 Ndipo ine ndinatuluka. Iye anali atagona pamenepo, kuyang’ana pa ine, kukhala ngati kuphethira maso ake, kuyang’anitsitsa. Ndipo ine ndinati, “Usiku wabwino.” Iye sanalankhule mawu. Ine ndinagwira dzanja lake. Ine ndinati, “Usiku wabwino.”

111 Nati, “Iye sakudziwa ngakhale dzina lake lomwe, M’bale Branham. Iye wakhala asakudziwa kwa zaka ziwiri.”

112 Ndipo ine ndinagwira dzanja lake. Ndipo mwa dalitso la Mulungu chabe zinachitika kuti ine ndinakhala wosamala. Iye anangondikoka ine ndi manja onse, monga *choncho*, ndipo iye akanakhoza mwina kuthyola mafupa a thupi langa. Ndipo ine ndinaponya mwendo wanga ndi kumumenya iye cha pachifuwa pomwe. Iye anangondikokera ine mpaka pansi. Ine ndinadzikoka mwamphamvu kwa iye. Ndiyeno pamene ine ndinali kumuthawa iye, kuti ndikafike pamasitepi, ine ndinawona chomwe ine sindinachiwonapo kale lonse. Mkazi ameneyo, miyendo yake iwiri ili mmwamba, monga *chonchi*, kubwera akundithamangitsa ine, ali chagada, ngati njoka. Umakhoza kumumva iye akukwawa chotero, pansi.

113 Tsopano, uyo ndiye mdierekezi. Inu munganene zina, zomwe inu mukukhumba, koma mkazi ameneyo anamangidwa ndi mdierekezi. Iye ankabwera kwa ine chagada, ngati serepente, ndipo iye anadzuka pamenepo ndipo iye anakadzimenyetsa ku mbali yina ya chipupa *chotero*. Iye anatembenuka, napondetsa miyendo yake yaikulu yamphamvu... anamenya monga *choncho*. Panali mpando uli pamenepo. Iye anawumenya iwo ndi mutu wake; magazi anatumphuka kuchokera mbali ya mutu wakeyo. Ndipo—ndipo iye anachotsapo kachidutswa kake. Ndipo iye anachigwira icho mu dzanja lake, nachiponyera icho kwa mwamuna wake ndipo chinakamenya chipupa. Ndipo pulasitala anagwa kuchokera pa chipupa, pamene iye anamenya ndi icho mwamphamvu yoteroyo... Wopenga; makumi awiri a mphamvu yake, mwina. Ndipo pamenepo wamkulu ameneyo... Iye anali wa usinkhu wabwino, mkazi wamphamvu, basi.

114 Ndiyeno iye anayamba kupanga phokoso lodabwitsa ndithu, kumati, “I-i-i-i-i, iiiiii,” ngati *choncho*. Ine ndinayang’ana pa iye, ndipo ine ndinaganiza, “Bwanji, ine sindinawone konse kanthu... Mulungu chitirani chifundo munthu wosauka womangidwa chotero!”

115 Ndipo mwamunayo anayamba kulira. Iye anayenda mpaka anakayika manja ake moyangata, mikono yake anandiyangata ine, nati, “M’bale Branham, tsopano inu mukuti palibe

kunjenjemera ayi?” Nati, “Ndipo ine sindikudziwa komwe ine ndingapite.” Iye anasweka mtima, mwa kulira. Iye anati, “Iye ali ndi ana asanu aang’ono kunyumba.” Ndipo anati, “Ine—ine . . . Iye wakhala ali mkazi wabwino.” Nati, “Iye ankagumula makande awa nandithandiza ine kusamalira mbewu ya thonje.” Ndipo anati, “Pamene iye anayamba kudwala,” anati, “Ine ndachita chirichonse chomwe ine ndikanakhoza kuchita. Ine—ine ndinagulitsa farmu yanga.” Ndipo anati. “Pofuna kuti ndimubweretse iye kuno, M’bale Branham, ine ndinali ndi chinthu chimodzi chotsalira, abulu awiri. Ndipo ine ndinawagulitsa iwo, kuti ndipeze m’bale womubweretsa iye mailosi mazana awiri, kumubweretsa iye mpaka kuno. Ndipo tsopano uyu waswa magalasi a galimotoyo, ndicho chifukwa chake miyendo yake ikuwukha magazi.” Nati, “Iye sanaleke kukhala chagada kwa zaka ziwiri, ndipo sakudziwa ngakhale dzina lake lomwe.”

Ine ndinati, “Chabwino, m’bale, zedi, Mulungu akhoza kumuchiritsa iye.”

¹¹⁶ Ndipo pafupi nthawi imeneyo mkaziyo anatembenuka. Iye anati, “William Branham, iwe ulibe kanthu kochita nane. Ine ndinamubweretsa iye kuno.”

Iye anati, “Motani . . .”

¹¹⁷ Ine ndinati, “Ameneyo si iye. Uyo ndiye mdierekeziyo akulankhula kuchokera mwa iye.” Izo nzolondola. Izo zikuzindikira. Izo zikudziwa.

¹¹⁸ Iye anati, “Motani, M’bale Branham, amenewo ndi mawu oyamba omwe walankhula mu zaka ziwiri.

¹¹⁹ Ine ndinati, “Mdierekezi akungogwiritsa ntchito milomo yake, chabe monga ujayu mu nkhani ya legio.”

¹²⁰ Iye anabwera akukwawira chotero kwa ine, nati, “Iwe ulibe kanthu kochita nane.” Kumakwawa ngati choncho.

¹²¹ Ine ndinati, “M’bale, kodi iwe ukukhulupirira nkhani yomwe iwe wandimva ine ndikunena za kubwera kwa Mngelo uja?”

¹²² Iye anati, “Ndi mtima wanga wonse,” iye ankanena, pamene iye ankayangata manja ake pa ine.

¹²³ Ine ndinayenda kumka ku sitepi yapakona, ndipo ine ndinapemphera ndi mtima wanga wonse, kwa Ambuye Yesu. Ine ndinati, “Mulungu, tayang’anani pa mkazi wosawuka uyo; ana asanu aang’ono osalakwa ali kunyumba, opanda mayi, mwana mmodzi woyamwa.” Ine ndinati, “Chingachitike ndi chiyani? O Mulungu, chitani chifundo!” Ndipo Mzimu wa Ambuye unabwera. Ndipo ine ndinafunsa mdierekezi kuti amsiye mkaziyo.

Kutembenukiranso mmbuyo, ine ndinati, “Tsopano kodi iwe ukukhulupirira zimenezo?”

124 Iye anati, “Ndi mtima wanga wonse. Kodi ine ndichite naye chiyani, M’bale Branham?”

125 Iye ndinati, “Mtenge ubwerere naye. Mtenge iye ubwerere naye ku chipatala cha openga.” Ine ndinati, “Ngati iwe siukukayikira chinthu chimodzi chomwe ine ndakuwuzwa iwe, uwone chomwe chiti chichitike.”

126 Miyezi iwiri zitachitika izi, ine ndinali ku Jonesboro, Arkansas, kumeneko kumene zinthu zambiri zinali kuchitika. Anthu zikwi makumi awiri ndi zisanu ndi zitanu ena atasonkhana mu mzinda. Ndipo ine ndinali kulankhula, ndipo ine ndinawona, akupereka kapena kugwedezera manja ake pa ine, mkazi wina. Iye anati, “Kodi inu simukundizindikira ine, M’bale Branham?”

127 Ine ndinati, “Ayi, mayi.” Iye anali atakhala kumeneko chotero, ndipo aliyense. . .

128 Nati, “Ine. . . Inu nonse, nonse inu ndikhululukireni ine.” Iye anati, “Ine ndimangofuna kukuwonani inu.”

129 Ndipo ine ndinawona wina akuseka; anali mwamuna wake. Ndipo iye anali atakhala pamenepo, ali bwinobwino basi ndi woganiza bwinobwino, palimodzi ndi ana ake aang’ono asanu, wangwiro basi monga momwe iye akanakhoza kukhala.

130 Iwo anali atabwerera naye. Iye sanayimenyenso galimoto nthawi imodzi, pobwerera. Iwo anamuyikanso iye mu ndende yokhomedwa. Mmawa wachiwiri, iwo analowa mkati kukamudyetsa iye, ndipo iye anali atakhala tsonga. Ndipo wachinayi wake, wachitatu kapena mmawa wachinayi, iwo anamutulutsa iye ngati munthu yemwe ali bwino, namutumiza iye kunyumba kwa ana ake. “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawi zonse.”

131 Yang’ana, mzanga, ziwanda zimazindikira Mphamvu ya Mulungu nthawizina atumiki asanati atero, ndi Akhristu. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Nthawi zambiri. Werengani Baibulo.

Pamene wansembe ananena izo, “O, Iyeyu ndi Bezebeule.”

132 Mdirekezi anati, “Ife tikudziwa Yemwe Inu muli, Mwana wa Mulungu, Woyerayo wa Israeli.” Kodi izo nzolondola? [Mpingo uti, “Amen.”—Mkonzil

133 Inu mukukumbukira pamene Paulo ndi Sila, pamene atumiki anati iwo anali onyenga? Wa m’bwebwe wokalamba uja anati iwo anali amuna a Mulungu, amene anali ndi njira ya Moyo.

134 Ngati ine sindikulakwitsa, M’busa Hooper, wochokera ku Phoenix, Arizona, wakhala kumbuyo kwa nyumbayi, iye akanakhoza kutsimikizira mfundo imeneyo. Kodi simunalipo inu usiku uja, M’busa Hooper? Pali mwamuna apo amene analipo kumeneko pamene izo zinkachitika. Lemberani kwa M’busa G.H. Brown, 505 Victory Street, Little Rock, Arkansas, ndipo

mumufunse iye za umboniwo. Muloleni iye akutumizireni inu . . . Aloleni a chipatala cha openga achitire umboni wa izi. Uwo ndi umodzi wa zikwi.

¹³⁵ Kamodzi kena kokha. Tsiku lotsatira kwa ili, Mngelo wa Ambuye anabwera mu nyumbayo. . . Ndiyeno ine ndiyamba mzere wa pemphero.

¹³⁶ Ine ndinali—ine ndinali komwe ku El Dorado. Ine ndi woti ndikhale ndiri kumeneko ku msewu wa mpikisano usiku uwiri; posachedwapa ine ndikangochoka kuno, ndikupita ku Shreveport, ndipo kenako ku El Dorado, ndi kumangopitirira. Ine—ine ndinali ku tchalitchi chaching’ono. Iwo anati, “Ngati inu mungabwere kudzalankhula ku tchalitchi ichi. . .”

¹³⁷ Zikwi zinaundana mu mzinda. Ndipo mtolankhani anatembenezidwa; pa chithunzi ichi, woyang’anira pa—pa hotelo; onsewo nthawi imodzi. Iwo ankafuna kudziwa momwe angampezere Yesu. Anakhala ali mamembala a mpingo kwa zaka; koma pamene iwo anawona ntchito ya Mulungu, yomwe Mulungu anali kuchita nayo, pakati pa anthu Ake. Iwo anali ndi ine mu ka—ka—kachipinda kakang’ono. Ndipo ine ndinali ndikulalikira.

¹³⁸ Ndipo pamene ine ndinatuluka kunja, panali amuna anyi anasonkhana chondizinga ine, anayamba kutuluka pakhomo. Ndipo choyima mu mvula kunjako, atagwirizira chirona pa mitu ya okonedwa awo ndi chirichonse, mtunda wa nyumba za mu mzinda, anthu akudikirira; kusowa malo oti nkupita, ayi, sakanakhoza ngakhale kulowamo, kopanda malo konse, kopanda nyumba za anthu. Iwo anali ndi manyuzipepala atayalidwa pansi, atagwirizira chirona, pamene mvula yamvumbi imavumba pamwamba pake, ana ang’ono opunduka, namayembekezera nthawi yawo kuti ayesere kukalowa mu mzere wa pemphero. Ine ndikuwuzani inu, m’bale, amenewo ndiwo anthu omwe amakonda Mulungu. Izo nzolondola. Ine sindidzayiwala konse. Zinthu zambiri zauzimu zopambana, zozizwitsa zachitika, mumzere. Ine ndinayambira kunja kwa nyumbayo, anthu akulira, kupanikiza, kuyesera kufika komwe iye anali, chotero. Iwo anali ndi mzere uwu ukusunthira molunjikira ku galimoto.

¹³⁹ Ine ndinkamvabe wina akufuula, “Chifundo! Chifundo! Chifundo!”

¹⁴⁰ Ndipo ine ndinayang’ana pozungulira. Ine ndinakhoza kuchimva icho penapake, kuwoneka ngati chinachake chikungodumphu mu mtima wanga. Ine ndinayang’ana. Kuyima potalikira ku mbali imodzi. . . Mu Arkansas iwo ali ndi—ndi lamulo, akuda ndi oyera sangathe kukhala palimodzi. Atayima cha kumbali imodzi anali bambo wachikuda, atangogwirizira kachipewa kakang’ono mmanja ake, atayima pamenepo mu

mvula, ndipo mvula ikumumenya iye mu nkhope. Mkazi wake akufuula, “Chifundo! Chifundo! Chifundo!”

¹⁴¹ Ine ndinaganizira za Bartumeyo wakhungu uja. Ndipo ine ndinayamba kupitirira, ndipo kuwoneka ngati Chinachake kumangondiwuza ine kuti ndisachite zimenezo. Mazana a iwo, akukankha. Ine ndinati, “Ine ndikufuna kupita uko komwe bambo wachikudayo ali.”

¹⁴² Iwo anati, “M’bale Branham, inu simungachite zimenezo.” Awiri a iwo anali apolisi. Iwo anati, “Inu mukhoza kuyambitsa mkangano wa mitundu pakali pano.” Nati, “Inu simungachite zimenezo.”

Ine ndinati, “Koma Ambuye akundiwuza ine kuti ndipite kumene iye ali.”

¹⁴³ Ndipo ine ndinangotulukira mbali yina ndi kupita cha kumeneko. Iwo anapanga kabwalo kakang’ono. Ndipo ine ndinamumva mkaziyo akunena, pamene ine ndinali ndikubwera; mkazi wachikulire, iye anati, “Awa akubwera abusa, okondedwa.” Mai, mai! Ndinakafika pafupi pang’ono ndi komwe iye anali.

Iye anati, “Kodi ameneyu ndi inu, M’busa Branham?”

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

¹⁴⁴ Iye anayamba kundisisita ine pa nkhope, ndi dzanja lake. Ndipo iye anati, “Abusa, kodi inu muli ndi miniti yokha kuti mumve nkhani yanga?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

¹⁴⁵ Iye anati, “Abusa,” iye anati, “mayi wanga achikalambire anali mkazi wachipembedzo chabwino.” Nati, “Iye sanandiwuzepo ine bodza mu moyo wake wonse.” Nati, “Iye wakhala atamwalira tsopano kwa zaka khumi.” Nati, “Ine sindinamvepo za inu m’moyo wanga wonse, ngakhale.” Nati, “Ine ndimakhala pafupi mailosi zana kuchokera kuno.” Ndipo anati, “Usiku wathawu...” Nati, “Ine ndakhala wakhungu tsopano kwa zaka zambiri.” Nati, “Usiku watha, ine ndinadzuka, ndipo atayimirira pambali pa bedi yanga anyaima mayi wanga wokalamba. Ndipo iye anati, ‘Wokondedwa, mwana, iwe upite komwe ku El Dorado, Arkansas, ndipo ukafunse za winawake dzina lake Branham.’ Nati, ‘Ambuye wapereka mphatso ya machiritso Auzimu. Iwe udzalandira kupenya kwako.’” O, mai, zikumveka ngati mtima wanga ukanafika pokula *chotero*. Ine ndinawona kuti Mulungu anali kulankhula.

¹⁴⁶ Ngati munthu sakhulupirira izi, Mulungu adzaziwonetsera izo njira yina kwa woona mu mtima. Iye adzatero.

¹⁴⁷ Ine ndinayika manja anga pa iye, ndipo ine ndinati, “M’bale, Ambuye Yesu amene watumiza masomphenya awa kwa iwe wayima pano tsopano kuti iwe ukhale bwino.” Ine ndinachotsa manja anga pa iye.

148 Ndinagwira dzanja lake; khungu linafa. Misozi inabwera ndikutsikira pa masaya ake. Iye anati, “Ine ndikuthokoza Inu, Ambuye. Ine ndikuthokoza Inu, Ambuye.”

Iye anati, mkazi wake anati, “Wokondedwa, kodi iwe ukupenya?”

Nati, “Inde, ine ndikupenya.”

Nati, “O, iwe—iwe ukupenyadi, wokondedwa?”

149 Nati, “Inde.” Nati, “Iyo ndi galimoto yofiyira ili apoyo.” O, mai! Iye anangoyamba kufuula chotero.

Ndiyeno iwo anandigwira ine, kunditengera ku galimoto.

150 Kenako, ine ndinali nditatsika ndege komwe pafupi ndi Memphis, Tennessee, usiku wina. Ine nditayamba kulowa, ine ndinamva winawake akufuula, “Moni, M’busa Branham!” Ine ndinapita komweko. Ndipo kodi anali ndani? Apo iye anali, wabwinobwino, amakhoza kuwerenga Baibulo lake kapena chirichonse.

151 Ine ndikuganiza, “Chisomo chodabwitsa, kukoma kwa liwu lake, lomwe linapulumsa wopanda pake. . .”

152 Iye anakali chimodzimodzi usiku uno monga Iye analiri nthawiyo. Iye ali pano, amzanga. Chinthu chokha chimene ine ndikukupemphani inu kuti muchite ndicho kukhulupirira kuti ine ndakuwuzani inu Choonadi. Ndipo yang’anani Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse pamene akuchita momwe ine ndakuwuzirani. Ngati Izo sizichitika, ndiye inu munene kuti M’bale Branham ndi mneneri wonama. Ngati Izo zichitika, ndiye inu mukhulupirire Mulungu chifukwa cha umboni Wake.

Tiweramitse mitu yathu.

153 Atate athu Akumwamba, o, ine ndikuganiza, tsiku lina pamene ife tidzafika pamapeto a ulendo, ndipo ine ndidzabwera ku nyumba Yanu, ine ndikupemphera kuti Inu mudzandirole ine kulowamo, ndipo ine ndikhoza kudzakhala penapake kumeneko kalimodzi ndi anthu onse okondedwa awa amene ine ndakumana nawo. Ife tikhoza kukambirana zinthu, zokumbukiridwa zomwe ife tirinazo za zinthu zazikulu izi zomwe Inu mwatichitira ife. Ndipo kudabwitsa kwake, popitirira mu ulendo wa osagonera kuno, kuti tikuwoneni Inu ndi kuzindikira kuti Inu muli pafupi, ndipo Inu muli pano usiku uno kudzawombola odwala awa ndi anthu osautsika.

154 Ambuye, mpaka nthawi iyi, ife sitikudziwa amene Inu mwawasankha kuti abwere mu mzere uwu. Inu mukuwadziwa. Winawake ali pano. Pali anthu makumi asanu amene ali ndi makadi. Ambuye, Inu mupereka. Inu mukudziwa yemwe ali pano kuti abwere. Ndipo ife tikudzipeka izi m’manja Anu, Ambuye.

155 Tsopano dalitsani aliyense. Ndipo mulole iwo, Ambuye, amene sakhoza kukhala mu mzere wa pemphero, pamene

iwo awona ena amene ali osawutsidwa ndi kuzunzidwa, monga iwo ali, kuwaona iwo atawomboledwa, O Mulungu, ine ndikupemphera kuti chikhulupiriro chawo chikwere mmwamba ndi kukhulupirira. Ndipo, O Atate, perekani kuti padzakhale chitsitsimutso chachikale kungoyamba mu mzinda wonse, Ambuye, kuti mpingo uliwonse udzakhale ndi zitsitsimutso ndipo miyoyo yotayika idzakhale ikubwera kudzalowa, kukhulupirira pa Mwana Wanu wokondedwa. Perekani ichi, Mulungu Wokondedwa.

¹⁵⁶ Tsopano, Atate. Inu mukudziwa ku—kufooka kwa munthu. Ndipo ife tikudziwa Mphamvu ya Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mutumize Mngelo Wanu, Mmodzi Amene anandipatula ine kuchokera mmimba ya mayi wanga, kundibweretsa ine mu moyo uwu, ndipo wandidzozera kwa cholinga ichi, ayimirire pano usiku uno. Mulungu Wokondedwa, nditapanga maneno aakulu awa molimba mtima, pamaso pa zikwi, ndi mazana a zikwi za anthu, Inu simunalepherepo konse ayi. Ndipo ine ndikudziwa kuti Inu simutilephera ife usiku uno, koma Inu mupereka usiku uno kuti tchimo lobisika lililonse la mu mtima liwuzidwe kwa anthu; matenda awo awuzidwe kwa iwo, ziwanda zomwe zikuwamanga iwo. Ndipo aliyense awomboledwa (kodi satero, Atate?) chifukwa ife tikudalira Inu ndi kukonda Inu ndi kukhulupirira Inu, ndi kupempha izi mu Dzina Lanu ndi kwa ulemerero Wanu. Imvani pemphero la wantchito Wanu tsopano, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁵⁷ Chabwino, osamalira za nzere wa pemphero tsopano. [M'bale abwera pa cholankhulirapo ndipo ati, "Ine ndikufuna iwo amene ali ndi makadi a pemphero kuyambira B 85, mpaka B 100, yimani mu mzere monga mwa nambala yanu kudzanja langa lamanja, ndi kumanzere kwanu, pa masitepe a nsanja. Kuyambira B 85, mpaka B 100. Wina aliyense akhale chikhali."—Mkonzi.]

¹⁵⁸ Nkukhoza kunena, pamene iye akundanditsa mizere, aliyense muno akudziwa...Ife tikuyesera kunena ichi, kuti inu mukhale momvera. Ife sitidzakhala ndi choyankha...Ine ndiyenera kunena ichi mwa lamulo lake, usiku uliwonse. Ine ndiribe choyankha kwa otsutsa aliwonse mu msonkhanowu. Zinthu izi zimachoka pa mmodzi kupita kwa wina, makamaka khunyu, ndi zina zake zotero. Ine ndawona anthu akubwera ku msonkhano, abwino mwangwiro; kuwona wakugwa ali pano, ndipo wakugwayo kutuluka ali bwino ndipo wotsutsayo kutuluka ali wopunduka. Ine ndawaona iwo akulowamo ochuluka monga makumi awiri ndi asanu ndi atatu nthawi imodzi, kugwa ndi khunyu, pansu. Mphamvu za ziwanda izi zidzapeza malo opitako.

¹⁵⁹ Ndipo, amzanga, limenelo ndi Baibulo. Ndi angati akudziwa kuti icho ndi chiphunzitsa cha Baibulo, tiyeni tione manja

anu. Uwu ndi mpingo wa Chipangano Chatsopano ukugwira ntchito. Kodi sichomwecho, amzanga? Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse ya kuwombola.

¹⁶⁰ Ndipo pamene iwo akuwandandika anthu, ine ndikuganiza iwo amene ali mu zikuku, iwo akungofuna inu kuti mukhale bata, iwo abwera kudzakutangani inu pamene iwo... Pamene nambala ya khadi yanu yakonzeka, iwo adza—iwo adzakuyitanani inu.

¹⁶¹ Tsopano ine ndikufuna aliyense kuti akumbukire ichi. Inu muli—inu muli olandiridwa nthawi zonse olandiridwa ku misonkhano, aliyense. Koma pamene ine ndikukufunsani inu kuti muwelamitse mitu yanu, inu muyenera kuwelamitsa mitu yanu. Ndiyeno pamene ine... musadzutse mutu wanu mpaka mutamwa ine ndikunena pa cholankhulira ichi, kapena M'bale Bosworth kuyimirira pano, kuti mudzutse mutu wanu. Ngati inu mutero tisanafike apo, ine sindikhala ndi choyankha pa chomwe chingachitike.

¹⁶² Bambo Hooper, akhala pafupi, iwo anali pa...Ine ndimakonda kumuwona wina motero, anakhalapo mu misonkhano ina. Iye anali ku Phoenix, Arizona, ndi ife, kumene mmodzi wa akulu a mzinda, atakhala mu msonkhano.

¹⁶³ Iye anati, “Chabwino, iyo ndi nkhani yabwino ya kuwerenga maganizo,” nati, “Ine ndidzango... Sikanthunso izo.

¹⁶⁴ Ine ndinapitirira kukhudzika ndi mwamunayo. Iye anali atakhala kumbuyo chakumanja kwanga. Ine ndinati, “Winawake chakumanja kwangaku, wakweza mutu wake.” Iye samalola kuweramitsa mutu wake.

Mmodzi wa othandizira anamuza iye, nati, “Weramitsani mutu wanu.”

Iye anali mkulu wa mzinda, kotero iye anati, “Ine sindikusowa kutero.”

Kotero, “Chabwino.”

Kotero iye anandibwezera ine mawu.

¹⁶⁵ Ine ndinali ndi mwana wamng'ono pamenepo, ndipo iye anali ndi pinifolo wa chovala yemwe anakutidwa ndi nsanza pa iye, kuyesera... Iye anali ali ndi khunyu; atachitapo kamodzi pa nsanja pomwepo. Nthawi zina pamene wakhunyu afika, zimangowagwetsa iwo nkumaphipha.

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, bwana, ine ndakupemphani inu. Ndi zokhazo ine ndingachite.”

¹⁶⁶ Ine ndinapemphera. Ine ndinati, “Mulungu, musalole mwana wosalakwa uyu kuvutika chifukwa cha mwana uyo... chifukwa cha bambo uyo, kusamvera kwake.” Ndinamsiya mwanayo. Bamboyo anangomwetulira ndi kumapitiriza.

¹⁶⁷ Pafupi masiku awiri kenako, iye anabwera...kuyamba kumva zachirendo, nati, “O, ndi ine chabe kuganiza zimenezo, basi.” Nati, “Kungoti ndi—kungoti ndi kulingalira kwanga, iko kukungotenga ubwino wanga.” Anayesera kudzigwedeza kwa izo.

¹⁶⁸ Tsiku limodzi kapena lotsatira lakelo, mabwana anamutenga iye mu tawoni, akungoyenda chozungulira. Pafupi masabata asanu ndi limodzi otsatira, iye anabwera... .

¹⁶⁹ Ine ndinali ndi msonkhano mu Charles Fuller...ndi Charles Fuller, uko mu Long Beach. Ngati ena a inu munali kumeneko, inu mukudziwa kuchuluka kwa omwe anali kumeneko. Kunali zikwi zenizeni mmenemo, atayimirira pokwera ndi potsika pa gombelo, koteru iwo...Iye sakanakhoza kulowa mkatimo.

Anapita ku Los Angeles, sakanakhoza kulowa mmenemo.

¹⁷⁰ Ndipo, potsiriza, Modesto. Mkazi wake, usiku wa mvula, anagwa mkanjira. Ndevu zinali zitakula pa nkhope yake, moyipa, kuwoneka mowopysa. Ndipo iye anali pamenepo. Nati, “M’bale Branham, chinachake chiyenera kuchitika.” Nati, “Iye—iye—iye sakutha, sangadye nkomwe. Ife sitingathe kumumedzetsa madzi iye.” O, iye ankawoneka mowopysa. Kukhala pamenepo, maso ake kumangoyang’anitsitsa.

¹⁷¹ Ine ndinalowa mkati. Iye anayamba kuti, “hummmm,” kumachoka kwa ine, monga *choncho*.

¹⁷² Ine ndinawuza iwo kuti akhome chitseko. Ndipo ife tinali otopa, tinali mu nyumba ya phwando la usiku wa Loweruka kumeneko, kwa maora, kuchita nao odwala. Ine ndinawauza M’bale Brown ndi M’bale Moore kuti akhome chitseko, kuti anthu asalowemo. Mkazi wake anali matope okhaokha chifukwa chakugwa mkanjira, ndipo anagwirira miyendo ya buluku langa. Ine sindikanakhoza ngakhale kusuntha. Iwo sakanakhoza kundiguza ine, iye atagwiritsitsabe, kuti ndipite kwa mwamuna wake.

¹⁷³ Kwa maminiti makumi anayi ndi asanu otsatirawo, icho chinamuchokera iye. Iye anayangata manja ake pa ine ndi kundikum bata ine. Kuvala chipewa pamutu wake chotero, kundigwira chanza, napita kwawo kukakhala mwamuna wabwino.

¹⁷⁴ Kukuuzani inu, amzanga, ngati ine ndikanakhala wotsutsa, ine sindikanakhala pafupi ndi chimene chikuchitikacho. Ine ndiri pano kukuthandizani inu ndipo osati kukulepheretsani inu. Chabwino, tsopano, ingokumbukirani zimenezo. Ngati inu mungakhale chiweramitsire mutu wanu, ngati chinachake chikanachitika, ndiye ine ndiri ndi choyankha pa chimenecho. Tsopano, inu simukanapanga nkhanu ndi zimenezo, chifukwa ine ndidzazidziwa izo inu mukabwera pano. Koma tsopano inu mungokhala omvera, khalani mu pemphero. Pamene ine ndikufunsani inu kuti muwelamitse mutu wanu, inu

mungokhala chiweramitsire mutu wanu. Inu munachita usiku wathawu, mwachikondi kwambiri. Ndipo inu chitani chinthu chomwecho usiku uno, chirichonse chikhala bwino. Inu muli. . .

Mizere yanu ikhale yokonzeka.

Tiweramitse mitu yathu tsopano kwa kamphindi.

¹⁷⁵ Atate, ine ndikuzindikira kuti—kuti iyi ndi nthawi yopambana. Ndi nthawi pamene ife timayima maso ndi maso ndi mdaniyo. Ndipo pano pali opunduka, osautsika, ndi anthu amene akufa. Pano pali anthu amene akuyima mu nzere, amene mwina ali ndi khansara kapena mwina ali ndi vuto la mtima. Ine sindikudziwa chomwe chalakwika ndi iwo tsopano. Koma Inu mumuza mtumiki Wanu. Ndipo ine ndikupemphera, Inu, kuti Inu mumuwombole wina aliyense wa iwo mwangwiro bwino. Ndipo Satana akhoze kutulutsidwa nthawi iliyonse, ndipo iye ayalutsidwe pamaso pa gulu lonse. Wina aliyense akhale mwachikondi, Ambuye, kugwirizana, Akhristu onse. Tikhale ndi msonkhano wopambana usiku uno. Mulole Mphamvu ya Mzimu Woyera ingosesa kupyola mnyumba ino, chiritsani aliyense amene ali mnyumba ino, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Tiyeni tiyimbe, kamodzi kokha, ngati inu mungafune.

Kungokhulupira. . .

Aliyense mwakumvera chabe monga inu mungakhazere kutero.

Zinthu zonse ndi zotheka, kungokhulupira;
Kungokhulupira, kungokhulupira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungokhulupira.

Ndikudabwa ngati ife tikanakhoza kuyimba iyo chotere tsopano:

Tsopano ine ndikukhulupirira. . .

¹⁷⁶ Ndi angati akukhulupirira izo? Kwezani dzanja lanu pamene muli kuyimba.

. . . tsopano ine ndikukhulupirira, (yamikani
Ambuye!)

¹⁷⁷ [Malo opanda kanthu pa tepi. Mzere wa pemphero wayamba—Mkonzi]. . . ali ndi khansara kapena vuto lachikazi. Ndipo kamphindi chabe; iwo awiri onse akugunda pafupi mofanana. [M'bale Branham akulekeza kaye.] Ndi vuto lachikazi, ndicho chomwe chiri. Izo nzolondola? Inde. Ndithudi. Ziri pafupi ngati khansara, ngakhale, icho ndi chomwe chiri. Moyo sunakhale ngati kama woyikidwa maluwa a kumasuka kwa inu, kodi watero? Ayi. Inu muli ndi mavuto ambiri. [Kutha kwa kujambula. Mzere wapemphero unapitirira.]



MATENDA NDI ZOSAUTSA CHA50-0100
(Diseases And Afflictions)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Januwale, 1950, ku Church Of The Open Door, ku Louisville, Kentucky, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1992 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org